

**LESSON 43**

<b>Chitsononkho</b>	empty cob	<b>KUTI</b>	
<b>Khoko</b>	husk, leaf, skin	-kolola	reap break off
<b>Mtondo</b>	mortar	-tonola	knuckle off grains
<b>Munsi</b>	pestle	-konola	pound maize
<b>Mphale</b>	pounded maize	-gaya	grind
<b>Gaga</b>	bran, husk	-khuthula	pour out
<b>Chimera</b>	malt, sprouted maize	-peta	winnow
<b>Mgaiwa</b>	flour from mill	-bviika	take out water
		-bvuuula	dip, put in water

**KUTI** as a verb has various meanings according to the context :

"say" : Mukuti chiyani? Anthu amati wolakwa ndine.  
 Nditi uyu osati uyo. Akakupatsa kanthu,, uziti: Zikomo!  
 Mfumu uja anayankha nati: Msonkhano udzakhala loweruka.

"think" : Ndinamlembera kalata ndipo ndina!i adzandiyankha.  
 Muli pano? kodi! Ine ndimati munapita kuulendo. thought  
 Inunso muma nwa moŵa! Ine ndinkati simukumwa. thought

"intend" : followed by the Subjunctive; "want", "be about":  
 Ndimati ndifunse. I would like to ask a question.

Ndimati nikuthandizeni Anati achoke dzulo, koma analephera.  
 Akati ayende ankayenda pansu. Gatu anati andilume koma anachita mantha.  
 Anati apite kuulendo pamene anayamba matenda.  
 Ndikati ndimuitane kumsonkhano, mwina sadzabwera.

We find a similar construction in the negative form (infix -sa):  
 it is an invitation to change one's mind :

Musati muchoke! (to somebody who is about to leave or wants to go away)  
 Asati abwerenso kuno! (supposing that he wants to come again)  
 Usati ukwatiwe naye mnyamata ameneyo!

Sometimes the verb **kuti** expresses an attitude or disposition, for instance  
 when it is followed by "ideophones" p. 98:

Ndinangoti chete. I just remained silent.  
 Mwanayu akumva chifuwa; angoti tsoko-tsoko. ... he coughs continually.

Ati! or Eti! (Note intonation) "isn't it" "don't you?" p. 45

Pano mpabwino ati! Nonse muli okondwa eti!

Ati with intonation — — "he says" "they say" "it seems":

Akufuna kupita kwao ati. Anamanga nyumba yokoma ati.

Ati... sometimes expresses intensity "extremely"; exclamation cf. Si p. 89

Ati mphepo kuzizira kwake! Dziko lino ati kukoma kwake!

**KUTI** is also found in the form of a Verbal Adjective **Woti, choti, yoti...**  
**Anampatsa dzina loti Fanesi. (: Anamtcha dzina lake Fanesi)**  
**Mawu oti "Basopo" atanthauza chiyani? What means the word Basopo?**

Reduplicated, it means "such-and-such," "so-and-so," "this or that" :

Tinazolowera kulima mwa njira yakuti yakuti...in such-and-such way:  
 Akakupatsani chakutichakuti, musaliwale kumthokoza.  
 Mungapite kwakutikwakuti, mudzamva mbiri yomweyo.  
 Akakuuzani zakutizakuti, musazimve.

Sometimes it introduces a new sentence: we may find 3 constructions:  
 the Subjunctive; the Infinitive n'ku-; the Infix -zi- p. 76

Ndinalibe ganizo loti ndimkwatire mtsikana ameneyo.  
 Sindipeza nthawi yoti ndicheze naye.  
 Palibe chifukwa choti muchite mantha.  
 Nthawi yakwana yoti ndiitule pansu ntchito.

Palibe chifukwa choti nkuchita mantha.  
 M'nyumba muno mulibe malo oti nkuyalamo mphasa ziŵiri.

Ndinaŵapatsa nzeru yoti azikhululukirana.  
 Anatipatsa lamulo loti aliyense azithandiza mnzake.

We should not use the Subjunctive if it is only a statement or a declaration:

Tsiku lamulungu ndi tsiku loti anthu sagwira ntchito.  
 Ndinalandira mthenga woti amayi anga ali kudwala matenda aakulu.  
 Chimene ndinganene ndi ichi chakuti inu mwakawa. This is what I can say:  
 Chondidabwitsa ine ndi ichi chakuti sanandiŵe kanthu. What surprises me.  
 Chondipira ine ndi ichi chakuti anachoka osalawira. What displeased me...

Osati.. "and not" p. 47: Muzigula malalanje, osati nthochi.

**CHABE** as a noun means "nothing, rubbish, something worthless":

Ndi chabe kumanga nkhekwe ngati mulibe chimanga. It is vain...

As an adjective, it has the same meaning "worthless, of bad quality":

Anandiphikira ndiwo zachabe. (: zopanda pache) p. 38

Anakwatiwa ndi mnyamata wachabechabe. good-for-nothing

An adverb, it means "just, only" p. 39: Ali ndi mwana mmodzi chabe.

Munthu uja sali mphunzitsi konse; ali munthu chabe. (: ...wamba)

Musataye nthawi pachabe! Anakasaka nyama ndipo anabwera chabe.

Mukupita kuti? — Kuyenda chabe. : Kungoyenda)

Proverb : Chakomachakoma pusi anagwa chagada.